# Makalasi opanda Mipanda

FUFUZANI – ZINDIKIRANI – PHUNZIRANI – KONDANANI

## Kumene kumakhala mileme

Phunziro **3**

**Zomwe tiphunzira sabata ino:**

- Kodi chisa ndi chani
- Mitundu ya malo okhala mileme
- Pamene mileme imagwiritsa ntchito malo okhala osiyanasiyana
- Zimene mileme imafuna m'nyumba yokhalamo



Moni kachiwiri anzanga, ndine Spike.

Mu phunziro ili ndikufuna ndikuuzeni kumene ine ndi anzanga timakhala. Mukuganiza kungakhale kuti? Mwinamwake munaonapo mleme ikukhala pafupi ndi nyumba yanu?
Kunali kuti? M'mtengo? muphanga? Nyumba? Kodi mileme inali itadzuka? Kodi anali okha? Kodi anali atakhala mozondoka? Tiyeni tione!

Mukawona chizindikiro ichi:



mufunika thandizo kuchokera kwa munthu wamkulu.

Musaiwale, chizindikiro cha pensulo chimatanthauza kuti ndi nthawi yanu yoti muchitepo kanthu!

Taphatikiza mawu onse atsopano pamndandanda kumapeto ngati chikumbutso!

### Mudzafunika:

- Mapensulo achikuda
- Mkasi
- Cello tepi
- Chingwe

## 1 Kodi chisa ndi chiyani?



Chisa ndi imene timati ndi nyumba ya mileme, ndi kumene mileme imakhala ndi kupumala. (Mbalame zili ndi zisa, mileme imakhala ndi mala awo okhala.) Aliyense amadziwa kuti mileme imauluka usiku, ndipo imagona masana, choncho kuti tigone bwino, timafunikira nyumba yamdima ndi yabata komanso yotetezeka.



Timafunikiranso malo abwino osakako - kwinakwake kuti tipeze zakudya zambiri zokoma. Mileme imatha kusaka kulikonse komwe ingapeze chakudya, kungakhale nkhalango, kumunda, m'mudzi, m'mphepete mwa mtsinje... Kodi mleme ingapezenso kuti tizilombo kape zipatso zabwino zoti idye?




Mofanana ndi inu anthu amene mumakonda kugula zinthu m'dera lanu, ife mileme timakonda malo athu osaka akakhala pafupi ndi malo anthu okhala. Tikufunanso njira yotetezeka kuti tikafike kumeneko!

**Mwachidule, mileme imafunikira zinthu zitatu kuti ikhale ndi moyo wathanzi:**


1. **Malo otetezeka okhalamo ndikupeza kugona**
2. **Chakudya chochuluka**
3. **Njira yotetezeka yofikira kumene timakhala ndi kumene timakadya**



**Mwaona, sitili osiyana kwambiri, inu ndi ine!**


Bats without Borders.org

Kwa inu!



**Ntchito 1 :**
**Kodi mungamalize misamphayi ndikuthandizira mleme kupeza malo ake okhala?**

yambani apa!



Ndithandizeni kupita kunyumba!



Bats Without Borders.org

# 2 Mitundu ya zisa za mileme

**Mileme imatha kukhala m'malo osiyanasiyana! Ndipo mitundu yosiyanasiyana imakonda nyumba zosiyanasiyana.**



Mileme ina imakonda kugona m'maphanga, imakhala mozondoka. Mnzanga Bella, yemwe ndi Mleme Wamphuno Yamizeremizere, amakhala m'phanga

Nthawi zambiri timasonkhana pamodzi mu "makoloni", nthawi zina m'magulu okwana masauzande! Mileme imakonda kucheza, ndipo nthawi zambiri timakhala pafupi ndi banja lathu lonse.
Mileme ina yazolowera kukhala pafupi ndi anthu, m'nyumba.



Nyenyezi ndi mleme wa ku Maurit ndipo imakhala m'manda koma imakhalanso m'mapanga kapena m'nyumba. Mwina mwawonapo mleme m'nyumba? M'nyengo ya chilimwe, malo a padenga ndi abwino komanso otentha, ndipo ndi abwino kulera tiana ta mileme. Mutha kupezanso mileme pansi pa matailosi a denga, m'mabowo pakati pa njerwa, kapena ngakhale m'galaja kapena m'chipinda chapansi cha nyumba. Mileme yaing'ono kwambiri, monga mileme ing'onoing'ono ya pipistrelle, imatha kulowa m'malo ang'ono ngati chala chathu chaching'ono! Mileme nthawi zambiri imakhala m'nkhokwe kapena nyumba zakale zomwe sizinagwiritsidwe ntchito... kapenanso ngalande zakale... (ngati palibe amene akuigwiritsa ntchito, bwanji?)

Mileme ina imangokonda kukhala m'mitengo, ngati mbalame!
Logan ndi mayi ake, Bongi ndi mileme wa makutu aatali aku Botswana ndipo amakhala m'phanga la mtengo.






Mitundu ina yamilime ing'onoing'ono imabisala m'mabowo opangidwa ndi nyama zina monga akagogoda, kapena pansi pa khungwa losakhomerera.



M'madera otentha monga kum'mwera kwa Africa, mileme ikuluikulu monga Aidoloni (mleme wamitundu yadya zipatso) imakhala mozondoka m'nthambi. Ngati muli ndi mwayi, mutha kuwawona atazondoka panthambi masana! Bhonasi kwa mileme ya zipatso: malo awo okhala amathanso kukhalanso malo odyera ngati mtengo womwe akukhalamo ndi mtengo wa mango!



Ndipo palinso malo ena amene anthu sangawaganizire koma mileme imakhalamo, monga mkati mwa ndodo za nsungwi ndi muchulu a chiswe! Mmodzi wa anzanga ndi pipistrelle ya nthochi, kodi mungayerekeze kumene iye amakhala?...Osati pakati pa nthochi koma anatsekeredwa m'kati mwa chubu chopangidwa ndi masamba okulungidwa a nthochi!

**Nthawi zina mileme imapezekanso m'malo osawadziwa monga m'phika ya tiyi ndi malaya, koma izi sizomwe tingatenge ngati malo okhalamo.**



KODI MUMADZIWA?

**Kodi mumadziwa? Kusiyana ndi mbalame, mileme singathe kumanga! zisa kapena mazenje.**
**Nthawi zonse amapezerapo mwayi pazomanga, kapena mabowo omwe alipo kale. Choncho musadere nkhawa mileme ikuwononga nkhuni, kapena denga lanu!**




**Ntchito 2:**

**Kodi ndi malo ati mwa awa omwe mukuganiza kuti mileme imakhalamo?**

**Ikani chizindikiro m'mabokosi omwe ali pafupi ndi mayankho olondola**

**Kwa inu!**



Masamba a nthochi ☐




Magalimoto ☐




Mitengo ☐



Milatho ☐




Muphanga ☐




Nyumba ☐



M'nyanja ☐



Mu bokosi la mileme ☐



Pabedi lako ☐



Migodi ☐



Bats Without Borders.org

# 3 Zofuna zosiyanasiyana nthawi zosiyana



Mileme imatha kukhala ndi zofuna zosiyanasiyana nthawi zosiyanasiyana pachaka (komanso nyengo kapena m'kati ma tsiku). Mitundu ina ya mileme, ikakhala ndi pakati, imakonda kukhala kumalo kwawo kuti izitenthedwa. Ndipo ana akabadwa amafunikira malo ofunda kuti nawonso azifunda pamene mayi awo ali kunja kukafuna chakudya. Malo amenewo amatchedwa kuti matenite kumene mileme yambiri yaikazi ndi ana awo amakhala pamodzi.



M'madera ozizira kwambiri, kumene nyengo yachisanu imakhala yozizira kwambiri moti simungauluke ndiponso chokudya chimakhala chochepa, mileme ina imakhala m'tulo. Izi zikutanthauza kuti kupuma ndi kugunda kwa mtima kumachepe ndipo amagona m'nyengo yonse yozizira. Pachifukwa ichi, amafunikira kukhala malo ozizira komanso abata. Ndi nyama ziti zina zomwe mumazidziwa zomwe zimagona nthawi yachisanu?

Mileme ina imasamukira kumalo ena atsopano kumene nyengo ili yotentha ndipo kuli zakudya zambiri. Uku kumatchedwa kusamuka. Kodi mumadziwa, kuti chaka chilichonse kumakhala kusamuka kwakukulu  kwa nyama zoyamwitsa padziko lonse? Mileme 10 miliyoni yamitundu ya udzu, monga Aidoloni yomwe ali pano imawuluka limodzi kupita ku Zambia kukadya mitengo ya mango.




Kum'mwera kwa Africa, n'zochepa zimene zimadziwika kuti mileme ina imagona nthawi yachisanu kapena ayi. Koma asayansi akuganiza kuti ena a iwo amapita ku " tope" m'nyengo yachilimwe pamene chakudya chili chochepa ndipo usiku n'kozizira kwambiri. Izi zikutanthauza kuti amagona mochuluka, koma osati mozama monga  m'mene amagonera m'nyengo yachisanu.

**N'zomvetsa chisoni kuti vuto lalikulu limene mileme imakumana nalo ndi kusowa nyumba zawo ndi malo osaka zokudya (asayansi amatcha zimenezi "kuwonongedwa kwa malo okhala"). Ichi ndichifukwa chake mileme timafunikira abwenzi, oti azitisamalira ife / kutilankhulira ndi kuteteza malo omwe timagwiritsa ntchito ngati nyumba, komanso malo omwe timapeza chakudya chathu.**

Bats without Borders.org

**Ntchito 3: Pangani nyumba ya mileme!**

**Dulani chithunzi cha Spike ichi, ndikuchichekenila!**
**Pezani malo oti mungapachike mileme yanu- izi zikhoza kukhala m'chipinda chanu chogona, panja pamtengo, m'galaja yanu kapena pashedi. Bwanji osapachika chingwe mmwamba ndikupachika mileme yanu pamenepo. Mwina tengerani dongosolo la phunziro ili kusukulu ndikupangitsa aliyense m'kalasi mwanu kupanga imodzi - lingalirani momwe denga la kalasi yanu lingawonekere bwino! Gwiritsani ntchito tepi kuti mupachike mleme yanu.**

Kwa inu!



Kongoletsani malo ogona a milime yanu - nanga bwanji kupachika zingwe kapena kujambula chakudya kuti mileme idye! Samalirani mileme kapena mileme yanu yatsopano!

# Kafotokozedwe ka mawu
## (mawu omwe taphunzira lero!)

**Koloni** - gulu la mileme yomwe imakhala pamodzi.

**Kungona nyengo yachisanu** - pamene nyama zina (kuphatikiza mileme) zimakhala ndi tulo tatikulu nthawi yozizira.

**Matenite** - malo omwe mileme yaikazi imasonkhana kuti ibereke ndi kulera ana awo.

**Chisa** - kwawo kwa mileme - pali mitundu yambiri yosiyanasiyana.



Ndikukhulupirira kuti mwaphunzira zambiri lero!
Tikuwonani sabata yamawa, kuti mudziwe zonse za komwe mileme imakhala!

Musaiwale; mayankho azochitikazo apezeka patsamba la Facebook la Bats Without Borders!